

· Swahili Al Bukhary (5/14) 3697 – anandilankhula Muhammad Bin Hatim Bin Bazi-i, anatiwaza Shathan, anatiuza Abdu Al AZIZ Bin [P15] Abi Salmah Al Maajshon, nkhani inachokera kwa Ubaidullah, kuchokera kwa Naafi, kuchokera kwa Ibn Umar (R.A), yemwe anati: (tinali munthawi ya M'neneri (S.A.W) tsikumufananiza Abubakar ndi wina aliyense, kenako Umar, kenako Uthman, ndipo timasiya maswahaba a M'neneri (S.A.W).

5- MUCHIKHULUPIIRO CHA MASHIA IBLISU NDI WABWINO KWAMBIRI KUPOSA UMAR (R.A):

· Anasindika Sheikh wawo Al Bahrany mwini wake wa "Tafseer Al Burhan", khomo 98, ndimutu woti "Ndithu Iblisu akakhala malo apamwamba kumoto kuposa Umar- kutanthauza kuti Umariyo akakhala pansipa Iblisu-". (Al Ma-aalim Al Zul-faa tsamba 324-325).

M'NENERI (S.A.W) AKUMPATSA NKHANI YABWINO UMAR (R.A) YOTI ALI NDI NYUMBA YACHIFUMU KU JANNAH IYE AKADALI MOYO:

· Nkhani inachokera kwa Anasi mwana wa Malik (R.A) anati: adanena M'thenga wa Mulungu (S.A.W) kuti: "ndinalowa ku Jannah, kuti nditere ndinaona nyumba yachifumu yomangidwa ndi golide, ndipo ndinafunsa kuti kodi nyumba imeneyi ndiyandani? Ndipo oyankha anati: ndiyam'nyamata wachiQuraysh, ndipo ndinaganiza kuti m'nyamatayo dineyo, koma nditafunsanso kuti angakhale ndani ameneyo? Anandiyankha kuti: ndi Umar Bin Al Khattab". [Anayilandira Al Tirmithy 3689 komanso Ahmad 11985].

Swahili Al Bukhary (5/10) 3679 – anatilankhula Hajjaj Bin Minhaal, anatilankhula Abdu Al Aziz Bin Al Maajshon, anatilankhula Muhammad Bin Al Munkadr, nkhani inachokera kwa jabir Bin Abdullah (R.A), anati: adanena M'neneri (S.A.W) kuti: ndinaona nditalowa ku Jannah, kuti nditere ndinakumana ndi Al Ramiswau, mkazi wa Abu Talhah, ndipo ndinamva mawu osisima, ndipo ndinafunsa kuti mawu amenewa ndi andani? Anati: ameneyotu ndi Bilal, ndinaonaso nyumba yachifumu pawalo pake pali mtsikana wantchito, ndiye ndinafunsa kuti kodi nyumba imeneyi ndi yandani? Anati: ndiya Umar, ndinafunsa kuti ndilowe ndikayione koma ndinakumbukira nsanje yako" ndiye Umar anati: ndizosatheka iwe Mtumiki wa Mulungu nsanjeyo ndikachitireni inu.

· Swahili Al Bukhary (5/10) anandilankhula Muhammad bin Al Salat Abu Jaafar Al Kufy, anatilankhula Ibn Al Mubarak, nkhani inachokera kwa Yunus, kuchokeranso kwa Al Zuhry, yemwe anati: anandifotokozera Hamzah kuchokera kwa Bambo ake kuti: Mthenga wa Mulungu (S.A.W) anati: "ndili mtulo, ndinamwa – kutanthauza mkaka - mpaka ndimaona kuyenderera kwake muchikhadabu kapena Al Khattab akanakhala m'neneri". [Anayilandira Al Tirmithy ndi Ahmad].

muzikadabu zanga, kenako ndinapereka kwa Umar" ndi anafunsa (onse): ndichifukwa ninji anapatsidwa koyambirira (amapambana ndi chani)? Anati: "Al Ilm (maphunziro)".

· Swahili Al Bukhary (5/11) 3684 – anatilankhula Muhammad Bin Al Muthna, anatilankhula Yahaya, nkhani inachokera kwa Ismael, anatifotokozera Qays, yemwe anati: adanena Abdullah kuti tikadali anthu amphamvube (oopedwa) kuyambira panthawi yomwe Umar analowa chisilamu.

· Adanena M'thenga wa Mulungu (S.A.W) kuti: "kukanakhala kuti padzapezekanso M'neneri wina pambuyo paine ndiye kuti Umar Bin

6- AL KHOMEINY AMUTEMBERERA MUAWIYAH BIN ABI SUFYAN (R.A):

Imamu wa Mashia Al Khomeiny ananena zokhudza swahaba wolemekezeka olemba wahayi amene ali Mu'awiyah Bin Abi Sufiyani (R.A): "Mu'awiyah anali akutsogolera anthu ake kwazaka makumi anayi (40), komatu palibe chomwe anazipezera yekha posakhala matemberero adziko lapansi komanso mavuto atsiku lomaliza". [Bukhu la Jihad Al Nafsi, lolembedwa ndi Al Khomeiny, P.18].

ANALETSA M'NENERI (S.A.W) KUWATUKWANA MASWAHABA OLEMEKEZEKA (R.A):

· Adanena Mtumiki wa Mulungu (S.A.W) kuti: "musatukwane

Maswahaba anga, musatukwane Maswahaba anga, ndikumulumbirira amene moyo wanga uli m'manja Mwake kuti ngakhale mmodzi mwainu akanati apereke (munjira ya Mulungu) golide ofanana ndi phiri la Uhud sakanafika m'lingo wa mmodzi waiwo ngakhale theka(hafu) yam'lingo wawo". [Anayilandira Al Bukhary 3673].

· Swahili Al Bukhary (5/28) 3764 – anatilankhula Al Hasn Bin Bishr, anatilankhula Al Muaafy, nkhani inachokera kwa Uthman Bin Al Aswad, kuchokera kwa Ibn Abi Malikah yemwe anati: Muawiyah anapemphera rakah imodzi ya witr pambuyo pa

· pemphero la Isha, izi zinkachitika kapolo wa Ibn Abbas ali pompo, mnyamata atafika kwa Ibn Abbas ndikumfotokozera adamuyankha kuti: Msiyeni (Muawiyah) chifukwa iyeyo ndithu ndithu anali swahaba wa Mtumiki wa Allah (S.A.W), ananenanso kuti: ndithu iyeyo ndi Faqih (wodziwa malamulo kwambiri).

· Musnad ya Ahmad "ط" Al Risalah (29/426) 17895 – anatilankhula Allie Bin Bahr, anatilankhula Al Walid Bin Muslim, anatilankhula Saeed Bin Abdu Al Aziz, nkhani inachokera kwa Rabiah Bin Yazid kuchokera kwa Abdu Al Rahman Bin Abi Umairah (1) Al Azdy, yemwe anti nkhani inachokera kwa M'neneri (S.A.W) kuti iyeyo anamutshula Muawiyah, ndipo anati: "Oh Allah muyikeni iyeyo kukhala owongola komanso ongolani kudzera mwa iye". Anthu ake ndi okhulupirika anthu angwiro. Anayilembanso Al Bukhary mu "Al Tarikh Al Kabeer" 5/240, Al Tirmithy (3842) komanso Ibn Abi Aaswim mu "Al Aahaad Wal Mathaany" (1129). Al Baany anayiyika kukhala hadith yabwino.

7- MASHIA AZAKA ZINO AKUMAKUTENGA KUTUKWANA MASWAHABA KUKHALA DINI KOMANSO KUTSATIRA M'NENERI (S.A.W) – LOMWELILIBODZA:

Adanena Sheikh wa Mashia: "Husein Al Khoraasany" mubuku lake lotchedwa "Chisilamu mudangalira la chishia" (Al Islam ala dhaw-u Al Tashayyu-u)" monama kuti: "ndizololedwa kwa Mashia kuwatemberera ma sheikh awiri; Abubakar ndi Umar ndiamene amawatsatira awiriwa. Ndithu anapanga izi (zololeza kutembererazi) potsatira Mtumiki wa Mulungu (S.A.W), komanso potengerera chitsanzo chake.

Anatinso: ndithu popanda chikayiko anthu amenewa ali othamangitsidwa pamaso pa M'neneri komanso otembereredwa ndi Allah Ta'ala kudzera mwa kazembe wake (S.A.W)". [Al Islam ala dhaw-u Al Tashayyu-i, P.88].

ANALAMULA M'NENERI KUMUTSATA ABUBAKAR NDI UMAR NDI MASWAHABA OLEMEKEZEKA (R.A):

· Adanena M'neneri wa Mulungu (S.A.W) kuti: "tengerani zochita za awiriwa pambuyo panga; Abubakar ndi Umar.....". [Anayilandira Ahmad ndi Al Tirmithy kuchokera kwa mwana wa Mas'ood anthu akenso okhulupirika].

· Adatinso M'tumiki wa Mulungu (S.A.W): "Abubakar ndi munthu wabwino, Umar ndi munthu wabwino, Abu Ubaidah Bin Al Jarraah...". [Anayilandira Al Tirmithy ndi Ahmad].

· Musnad Ahmad "ط" Al Risaalah (38/399) 23386 – anatilankhula Muhammad Bin Ubaid, anatilankhula Salim Al Muraady, nkhani inachokera kwa Amru Bin Harm Al Azdy, kuchokeranso kwa Abi Abdullah ndi Rabaiy Bin Haraash, kuchokera kwa Huthayfah anati: pamene ife tinali kwa Mtumiki (S.A.W) anati: "ine sindikudziwa nthawi yomwe yatsala yokhala nanu, ndiye mudzatengere zochita za awiriwa pambuyo panga – amalozera kwa Abubakar ndi Umar – mudzatengerenso chiongoko cha Ammar ndi malangizo a Ibn Umami Abd".

8- UDZUDZU NDIWABWINO KWAMBIRI KWA MASHIA KUPOSA MA SWAHABA A M'NENERI (S.A.W) AMENE ANAMUTETEZA NDI KUMPATSA MALOIYE:

Ananena m'modzi mwa Masheikh akuluakulu a Mashia Muhammad Hussein Aal Kashif Al Ghitwai: "ndithu zomwe akumasimba — mwachitsanzo Abu Hurayrah, Samurah Bin Jun-dub ndi Amru Bin Al Aaswi ndi anzawo ena onga omwewa anthu amenewa alibe mulungo uliwonse ngakhale ofananirapo ndi udzudzu kugulu la Imamiyyah". [Aswitu Al Shia wa usuliha, P.79].

QUR'AN IKUWAYIKIRA ULEMERERO WAWUKULU OMWE ADATSOGOLERA KULO WA CHISILAMU MAKKA ISANAGONJETSSEDWE, YAWAYIKANSO IWOWA KUKHALA AKULUAKULU AASILAMU (R.A):

· Allah Ta'al akunena kuti: ".....Sali ofanana mwa inu amene adapereka chuma (panjira ya Mulungu) pamodzi ndi kumenya nkondo usadagonjetsedwe mzinda wa Makka, iwowo ndi omwe ali ndi ulemerero waukulu kuposa amene apereka chuma chawo ndi kumenya nkondo pambuyo. Koma onsewo Mulungu wawalonjeza zabwino, ndipo Mulungu akudziwa zones zimene muchita". [Al-Hadid 10].

· Adanenanso M'tumiki wa Mulungu (S.A.W) kuti: "anthu abwino kwambiri ndi omwe uli mu m'bado wanga uno, keneko m'bado otsatira wangawu, ndipo kenako, m'bado wotsatira pa otsatirawo". [Anayilandira Al Bukhary 3650 komanso Muslim 2535].

9- BODZA LA MASHIA LOTI ABUBAKAR NDI UMAR NDI GWERO LAKUSOCHERA KWA UMMAH:

Akunena Sheikh wama Shia Abd Al Hussein Al Murshty kuti: ndithu Abubakar ndi Umar awiriwa ndi gwero lakusochera kwa Ummah uno mpaka tsiku lakiyama". [Kashifu AL Ishtihabi P, 98].

ULEMELERO WA ABUBAKAR NDI UMAR KWA M'TUMIKI KOMANSO KWA ASILAMU (R.A):

· Nkhani inachokera kwa Jabir Bin Abdullah (R.A) adati: Adanena M'tumiki wa Allah (S.A.W) kuti:

"Abubakar ndi Umar muchipembedzo ichi ali ngati m'mene aliri makutu ndi maso m'mutu".

(Inayikidwa kukhala hadith yabwino ndi Al Baany mu Sahihah).

· Adanena M'thenga wa Mulungu (S.A.W) kuti: "ndithu eni masitepe apamwamba adzikaona omwe ali

pamwamba pawo munga m'mene mumaonera nyenyezi yowala m'chizime chakumtambo, ndikuti Abubakar ndi Umar ali m'gulu limeneli (la apamwamba) komanso ali ndi zabwino zoonjezera". [Anayilandira Al Tirmithy].


· Adanenanso M'tumiki wa Allah (S.A.W) kuti: " ndisamaleni ine kudzera mwa maswahaba anga, keneko m'bado otsatira wangawu, ndipo kenako, m'bado wotsatira pa otsatirawo". [Sunanu Ibn Maajah].

UTHENGA KWA ENI KUYANDIKITSA:

Pambuyo powonetsa zikhulupiliro zachishia, ndithu munthu atha kukhala odabwa kuwadabwa omwe akuyitanira kuchiyanjano ndi Mashia ponena kuti palibe kusiyana muzikhulupiliro pakati pa Asilamu ndi Mashia komwe kungaletse kuyandikana pakati pawo. Zitheka bwanji kuyandikana ndi anthu amene amakhulupilira ukafiri wa anthu abwino pambuyo pa atumiki ndi aneneri; maswahaba (ophunzira) a M'neneri (S.A.W). Ndipo akumawatukwananso abwino kwambiri mwaiwo; imvani ndipo dziwani kuti amenewatu ndi Abubakar, Umar ndi Uthman (Ridhuwanullah Alayhim).

www.islamic-invitation.com

www.alburhan.com



CHIKHULUPIIRO CHA MASHIA PANKHANI YOKHUDZA MASWAHABA (R.A)



Conveying Islamic Message Society
P.o.Box 834 - Alex - Egypt
E-Mail: info_en@islamic-message.net
E-mail: cims_eg@yahoo.com
Site: www.islamic-message.net
Not for sale
نهيرو ولا يبيع

بلغة الشيشيو

Mukakalata kathumu tiyamba ndikuona chikhulupiliro cha mashia ndinso chikhulupiliro cha Asilamu paza anthu abwino pambuyo pa atumiki ndi aneneri, maswahaba a M'tumiki wa Mulungu madalitso ndi mtendere wa Mulungu ukhale paiye (S.A.W), maswahaba ake amene Mulungu powayeretsa iwo anabvumbulutsa Qur'an yomwe idzakhala ikuwerengedwa mpaka kufika kwa nthawi (kiyama).

QUR'AN INAYAMIKIRA MASWAHABA AM'NENERI (S.A.W)

1. Allah Ta'ala akunena za maswahaba olemekezeka (R.A) kuti: “Ndipo amene adatsogolera poyamba, am'gulu la mamuhajirina ndi answari, ndi omwe adawatsatira iwo mwaubwino, Mulungu adzakondwa nawo. Naonso adzakondwera naye (pa zomwe adzapatsidwe ndi Mulungu). Ndipo wawakonzera minda yomwe mitsinje ikuyenda pansi pake; adzakhala m'menemo muyaya.Uko ndikupambana kwakukulu”. [At-Taubah 100].

2. Allah Ta'ala akunenanso kuti: “Malipiro awo kwa Mbuye wawo, ndi minda yamuyaya momwe ikuyenda pansi pake mitsinje; adzakhala m'menemo muyaya Mulungu adzakondwa nawo, nawonso adzakondwa Naye (pa zomwe adzapatse), zimenezo ndi zayemwe awope Mbuye wake (Mulungu)”. [Al Bayyinah 8].

3. Akunenanso Allah Ta'ala kuti: “Mwa okhulupirira alipo amuna ena amene adakwanitsa zomwe adamulonjeza Mulungu (kuti sadzathawa pankhondo pamodzi ndi M'tumiki (S.A.W), ena mwa iwo adamaliza moyo wawo (nakwaniritsa lonjezo lawo pofera panjira ya Mulungu), ndipo ena mwa iwo akuyembekezerabe (kufera panjira ya Mulungu), ndipo sadasinthe konse (lonjezo lawo)”. [Al-Ahzaab 23].

4. Akunenanso Allah Ta'ala paza maswahaba amene akutchedwa kuti eni mtengo; maswahaba amenewa analipo okwanira 1400: “Ndithu Mulungu adasangalala nawo okhulupirira pamene amagwirana nawe chanza pansi pa mtengo pomwe amakalonjeza kuti (kuti adzamenya nkhondo mpaka imfa), Mulungu adadziwa zomwe zidali m'mitima mwawo ndipo adatsitsa pa iwo kukhadzikika (ndi kudekha) ndipo adawalipira kupambana kwapafupi”. [Al-Fath 18].

CHIKHULUPIIRO CHA MASHIA CHOSEMPHANA NDI QUR'AN:

komatu Mashia amakhulupilira zoti Maswahaba onse anatuluka chisilamu kupatula ochepa– atatu kapena anayi kapena asanu ndi awiri = mosemphana ndi mariwaya awo abodza = Ndipo amadziyandikitsa kwa Mulungu powatemberera, powatcha kuti makafiri ndi kuwada amene ali abwino kwambiri mwamaswahaba; amenewa ndiwo Abubakar Assiddik, Omar Bin Al Khattab, Uthman Bin Affan, Al Zubeir Bin Al Awwaam ndi Tal-hat Bin Ubaidullah(R.A)!!!

Koma kuti kugamula kwathu paza Mashia kukhale kwachilungamo tiyenera kudziwa zikhulupiliro zawo kudzera mumaphata mwawo zomwe amatengera chipembezo chawo, osati kudzera muzomwe zimangonedwa zokhudza iwowa.

M'bale wanga wokonedwa, tsopano ndikubweretserani zina mwa zikhulupilirozi ndi kuziyankha kwake kuchokera mu Qur'an ndi Sunnah:

1- CHIKHULUPIIRO CHA MASHIA PA ABUBAKAR NDI OMAR (R.A) CHOTI AWIRIWA NDI MAKAFIRI:

Nkhani inachokera kwa Bambo a Allie Al khurasany amenewa akuti nkhani inachokera kwa kapolo wa Allie mwana wa Al Hussein Iye anati: “ndinalinaye limodzi mtendere ukhale paiye munthawi zina zomwe amakhala payekha ndiye ndinati kwayie:

ndithu ine ndili ndi ufulu kwa inu, kodi simungandiwuze zokhudza amuna awiri amenewa; zokhudza Abubakar ndi Omar? Ndiye anati: awiriwa ndimakafiri, makafirinso amene angawakonde awiriwa”. (Biharu Al An-waar 72/137-138).

CHIKHULUPIIRO CHA ASILAMU PANKHANI YOKHUDZA MASWAHABA OLEMEKEZEKA (R.A):

· Swahih Al Bukhary (5/8) 3673 – anatilankhula Adam Bin Abi Iyaas, anatilankhula Shu'ubah, nkhani inachokera kwa Al A'mash, anati: ndinamumva Thak-wan, akulankhula nkhani yomwe inachokera kwa Ibn Saeed Al Khudriyy (R.A) adati: adalankhula M'neneri (S.A.W) kuti: “musatukwane Maswahaba anga, chifukwa

ngakhale mmodzi mwainu akanati apereke (munjira ya Mulungu) golide ofanana ndi phiri la Uhud sakanafika m'lingo wa mmodzi waiwo ngakhale theka (hafu) yam'lingo awo”.

ADALANKHULA M'THENGWA WA MULUNGU (S.A.W) PAZOKHUDZA MASWAHABA OLEMEKEZEKA (R.A):

· Swahih Al Bukhary (5/4) 3655 – anatilankhula Abdu Al Aziz Bin Abdullah, anatilankhula Sulaiman, nkhani inachokera kwa Yahaya Bin Saeed yemwe anyilandira kuchokera kwa Naafi' yemwenso anyilandira kuchokera kwa Ibn Umar (R.A) anati: “tinali tikusankha wabwino mwa anthu munthawi ya M'tumiki (S.A.W) ndiye timasankha Abubakar keneko Umar Bin Al Khattab keneko Uthman Bin Affan (R.A).

· Swahih Al Bukhary (5/5) 3662 – anatilankhula Ma'aly Bin Asad, anatilankhulanso Abdu Al Aziz Bin Al Mukhtaar, adanena Khalid Al Hithau, anatilankhhula anatilankhula kuchokera kwa Bambo a Uthman, anati: anandiuza Amru Bin Al Aas (R.A) kuti: “ndithu M'neneri(S.A.W) anamutumiza iye ndi asilikali kunkhondo yotchedwa “Thatu Al Salaasil” anati: ndiye ndinamufikira iye ndikumufunsa kuti ndindani amene ali okondeka kwambiri kwayie? Ndiye anati: “Aishah”, ndinafunsanso kuti nanga mwa azibambo? Anati: “Bambo ake, ndinati: kenako ndani? Anati: kenako Umar Bin Al Khattab ndiye anawawerenga azibambo”.

ndinati: kenako ndani? Anati: kenako Umar Bin Al Khattab ndiye anawawerenga azibambo”.

Swahih Al Bukhary (5/7) 3671 – anatilankhula Muhammad Bin Kathir, anatifotokozera Sufyan, antilankhula Jaami' Bin Abi Rashid, anatilankhula Abo Ya'ala, nkhani inachokera kwa Muhammad Bin Al Hanafiyyah, yemwe anti: ndinati kwa bambo anga: kodi munthu wabwino pambuyo pa M'tumiki (S.A.W) ndi ndani? Anati: Abubakar, ndinati: kenako ndani? Anati: kenako Umar, ndinaopa kuti angamutchule Uthman ndiye ndinangonena mofunsa kuti kenako inu eti? Anayankha kuti: ine sindili kanthu koma munthu wochokera mwa asilamu.

· Nkhani inachokera kwa mwana wa Mas-ood (R.A) amene anati: ndithu M'tumiki wa

Allah (S.A.W) anati: “ atulukira pakati painu munthu yemwe ali mugulu la anthu aku Jannah, nthawi yomweyo anatulukira Abubakar, kenako M'tumiki anatinso atulikira pakati panu munthu yemwe ali mugulu la anthu aku Jannah ndiye panatulukiranso Umar”. [Hadithiyi inalandiridwa ndi Al Tirmithy 3695].

· Nkhani inachokera kwa Allie mwana wa Abu Talib (R.A) anati: ndithu Mtumiki

(S.A.W) anamuyang'ana Abubakar ndi Umar ndipo anati: “awa awiriwa ndi mabwana a anthu achikulire (azibambo) aku Jannah, kuyambira mibado yoyambirira ndi yotsirizira

kupatula aneneri ndi atumiki”. [Inalandiridwa ndi Al Tirmithy 3666].

· Swahih Al Bukhary (9/5) 3675 – anandilankhula Muhammad Bin Bishar, anatilankhula Yahaya, nkhanin inachokera kwa Saeed yemwe anyilandira kuchokera kwa Qatadah kuti Anas Bin Malik (R.A) anawafotokozera iwowa kuti M'neneri (S.A.W) anakwera Uhud pamodzi ndi Abubakar, Umar ndi Uthman ndipo phiri la Uhudilo linagwedezeka Mtumiki anati (kuliwiza phirilo): “khazikiza iwe a Uhud chifukwa pamwamba pako pali M'neneri, mnzake, ndi mashahid awiri”.

2- MASHIA ANAPANGA DUWA YA MASWANAMU AWIRI A MAQRAYSH POTEMBERERA ABUBAKAR NDI UMAR (R.A):

Duwa yamaswanamu (mafano) awiri ama Quraysh mu Duwamu amamutemberera Abubakar ndi Umar (R.A) ponena kuti: “Oh Allah, tembererani mafano awiri ama Quraysh, asatana awo awiri, zopembezedwa zawo ziwiri, zopeka bodza zawo ziwiri, ana achikazi a awiriwa, awiri ake amene ananyozera lamulo lanu, anakanira chibvumbulutso chanu, anakanira mtendere wanu, ananyoza Mtumiki wanu, anatembenuza chipembezo chanu, analisokoneza buku lanu, anawononga malamulo anu ndipo adasokoneza mafaradh (malamulo achikakamizo) anu”. (Munawwar Hussein/Tuhfatu Al Awaami maqbul, P. 423-424).

MAWU A M'NENERI (S.A.W) PAZAYEMWE ANGATUKWANE MASWAHABA (R.A):

· Swahih Al Bukhary (5/8) 3673 – anatilankhula Adam Abi Iyaas, anatilankhula Shu'ubah, nkhani inachokera kwa Al A'mash, anati: ndinamumva Thak-wan, akulankhula nkhani yomwe inachokera kwa Ibn Saeed Al Khudriyy (R.A) adati: adalankhula M'neneri (S.A.W) kuti: “musatukwane Maswahaba anga, chifukwa

ngakhale mmodzi mwainu akanati apereke (munjira ya Mulungu) golide ofanana ndi phiri la Uhud sakanafika m'lingo wa mmodzi waiwo ngakhale theka (hafu) yam'lingo wawo”. Swahih Muslim (4/1967)2540.

· Nkhani inachokera kwa mwana wa Abbas (R.A) yemwe anati: Mtumiki wa Mulungu (S.A.W) adati: “munthu amene angatukwane maswahaba anga ayenera kupeza temberero la Mulungu, la angelo komanso ndi temberero la anthu onse”. [Hadithiyi inalandiridwa ndi Al Twabrany mu buku lotchedwa Al Kabeer kuchokera kwa mwana wa Abbas, Al baany anayiyika hadithiyi mugulu la mahadith abwino mu buku lotchedwa swahih Al Jaami-i (5111)].

· Nkhani inachokera kwa mwana wa Umar (R.A) yemwe anati: adanena M'tumiki wa Mulungu(S.A.W) kuti: “Allah amamutemberera munthu amene watukwana maswahaba anga”. [Inalandiridwa ndi Al Twabrany mu buku la Al Kabeer kuchokera kwa mwana wa Umar, inayikidwa kukhala hadithi yabwino ndi Al Baany mu buku lotchedwa swahih Al Jaami-i (5111)].

ndinamumva Thak-wan, akulankhula nkhani yomwe inachokera kwa Ibn Saeed Al Khudriyy (R.A) adati: adalankhula M'neneri (S.A.W) kuti: “musatukwane Maswahaba anga, chifukwa

ngakhale mmodzi mwainu akanati apereke (munjira ya Mulungu) golide ofanana ndi phiri la Uhud sakanafika m'lingo wa mmodzi waiwo ngakhale theka (hafu) yam'lingo wawo”. Swahih Muslim (4/1967)2540.

· Nkhani inachokera kwa mwana wa Abbas (R.A) yemwe anati: Mtumiki wa Mulungu (S.A.W) adati: “munthu amene angatukwane maswahaba anga ayenera kupeza temberero la Mulungu, la angelo komanso ndi temberero la anthu onse”. [Hadithiyi inalandiridwa ndi Al Twabrany mu buku lotchedwa Al Kabeer kuchokera kwa mwana wa Abbas, Al baany anayiyika hadithiyi mugulu la mahadith abwino mu buku lotchedwa swahih Al Jaami-i (5111)].

· Nkhani inachokera kwa mwana wa Umar (R.A) yemwe anati: adanena Mtumiki wa Mulungu(S.A.W) kuti: “Allah amamutemberera munthu amene watukwana maswahaba anga”. [Inalandiridwa ndi Al Twabrany mu buku la Al Kabeer kuchokera kwa mwana wa Umar, inayikidwa kukhala hadithi yabwino ndi Al Baany mu buku lotchedwa swahih Al Jaami-i (5111)].

3- MASHIA AKUONA KUTI MASWAHABA ONSE ANATULUKA CHISILAMU (R.A):

Nkhani inachokera kwa bambo a Jafar ananena kuti: “anthu onse anatuluka chisilamu pambuyo pa M'neneri (S.A.W) kupatula atatu, ndiye ndinati: atatu amenewa ndi ati?

Anati: Al Miqdadu Bin Al As-wad, Abu Tharri Al Ghifarry ndi Salmaan Al Faarisy”. (Rijaalu Al Kishy P.6. Al Kaafy 8/245).

CHIKHULUPIIRO CHA ASILAMU NDI CHAKUTI AMENE ANGAZUNZE MASWAHABA NDIYE KUTI WAZUNZA MULUNGU NDI MTUMIKI WAKE(S.AW):

· M'tumiki wa Allah (S.A.W) adati: “Opani Mulungu! Opani Mulungu! Pamaswahaba anga, musadzawatenge kukhala chochitira chandamale chotukana pambuyo panga. Ndipo amene wawakonda iwo ndiye kuti awakonda chifukwa chondikonda ine.Ndipo amene awada, ndiye kuti awada chifukwa chondidine. Amene angawazunze iwo ndiye kuti andizunza ine, tsopano amene angazunze ine ndiye kuti akhala ngati akuzunza Allah, ndipo ozunza Allah, Allah amampatsa chilango”. [Anyilandira Ahmad mu buku lake lotchedwa Al Musnad (8/4) komanso Al Tirmithy].

KUGAMULA KWA M'NENERI (S.A.W) KUTI MASWAHABA NDI ANTHU ABWINO:

· Swahih Al Bukhary (3/171) 2652 – anatilankhula Muhammad Bin Kathir, anatifotokozera Sufyan, nkhani inachokera kwa Mansour, yemwe anyilandira kuchokera kwa Ibrahim kuchokeranso kwa Obaidah, iye anyilandira kuchokera kwa Abdullah (R.A), iyeyu anyilandira kuchokera kwa M'neneri (S.A.W) Yemwe anati: “

Anthu abwino kwambiri ndi omwe ali mum'bado wanga uno, keneko m'bado otsatira wangawu, ndipo kenako, m'bado wotsatira pa otsatirawo, keneko kudzabwera anthu omwe m'modzi mwa iwo kuyikira umboni kuzidzaposa kulumbira kwawo, komanso kulumbira kwawo kuzidzaposa kuyikira umboni kwawo”. Ibrahim anati: (ndiye anali akutimenya tikayikira umboni wabodza kapena pangano). [Swahih Muslim (4/1963)2533].

4- KUSALEMEKEZEDWA KWA UTHMAN MWINI KUWALA KUWIRI, MAMUNA WAANA AWIRI A MTUMIKI(S.A.W) NDI MASHIA:

Mashia amanama kuti M'neneri (S.A.W) ndiamene anamutcha mwini kuwala kuwiri Uthman Bin Affan (R.A) dzina loti (Na-athal), zimenezi zili“ Muriwayah” lomwe mawu ake akuti: “ndithu Aishah adanena kwa Uthman kuti: Oh iwe Na-athal, iwe m'dani wa Mulungu, anakutcha iwe M'thengwa wa Mulungu (S.A.W) dzina la Na-athal, M'yuda waku Yemen". (Bihaar Al An-waar 31/297).

Monganso m'mene amakhulupilira kuti iyeyu ndiamene anapha mwana wankazi wa M'neneri (S.A.W). Nkhani inachokera kwa bambo a Jaafar (A.S) potanthawuza mawu a Allah Ta'ala oti: “kodi akuganiza kuti palibe amene angamuthe?” Abu Jaafar Anati: Ayayi ikutanthauza Na-athal chifukwa chakupha kwake mwana wa M'neneri (S.A.W). (Bihaar Al An-waar 9/252).

M'NENERI (S.A.W) AMUKWATITSA MWANA WAKE WAM'KAZI WACHIWIRI NDI UTHMAN (R.A):

Mukakalata kathumu tiyamba ndikuona chikhulupiliro cha mashia ndinso chikhulupiliro cha Asilamu paza anthu abwino pambuyo pa atumiki ndi aneneri, maswahaba a M'tumiki wa Mulungu madalitso ndi mtendere wa Mulungu ukhale paiye (S.A.W), maswahaba ake amene Mulungu powayeretsa iwo anabvumbulutsa Qur'an yomwe idzakhala ikuwerengedwa mpaka kufika kwa nthawi (kiyama).

· Pamene M'neneri (S.A.W) anabwerera ku nkhondo ya Badr anadziwa kuti mwana wake Ruqayyah wamwalira ndipo anadandaula kwambiri.Anamutonthoza Uthman (R.A). Ndipo kenako anamukwatitsa mwana wake wachiwiri (Ummu Kluthum) ndipo mmawu ake anati:

“ ndikanakhala kuti ndiri ndi mwana wachitatu ndikanamukwatitsanso ndi Uthman. Namutcha kuti mwini kuwala kuwiri chifukwa chokwatira ana awiri a M'neneri (S.A.W). Izi sizidachitike kwa wina koma kwa Uthman yekha.

· Adanena M'neneri (S.A.W) pazokhudza Uthman Bin Affan kuti: “kodi ine ndisachite naye manyazi munthu amene angelo amachita naye manyazi”.

· Nkhani inachokera kwa Anasi mwana wa Maliki (R.A) anati: adanena M'neneri (S.A.W) kuti: “ munthu amene ali wachifundo kwambiri mu ummah wanga ku ummah wanga ndi Abubakar, olimba kwambiri mwa iwo pa lamulo la Mulungu ndi Umar, wamanyazi kwambiri mwa iwo ndi Uthman ndipo odziwa kuweruza kwambiri mwa iwo ndi Ali”. [Inalandiridwa ndi Ahmad komanso Al Tirmithy].

· Swahih Al Bukhary (5/13) adalankhulanso M'neneri (S.A.W) kuti: “yemwe angakumbe chisime cha “Romah” akhala ndi Jannah”. Uthman ndi amene anakumba.Adalankhulanso kuti: “amene angapange gulu lankhondo yamatsautso kukhala tayale akhala ndi Jannah”. Ndipo Uthman ndi amene analipanga gulu lankhondo limenelo.